Kudandaula kwa Ombudzimani

Mosayang'ana kuti uyu ndi mamuna kapena wamkazi, mtundu, chikhalidwe kapena kochokera, munthu wina aliyense ali ndi ufulu odandaula ku ofesi ya ombudzimani ngati waona kuti walakwilidwa ndi nthambi kapena ogwira ntchito aliyense wa boma.

Kuti chidandaulo chilichonse chitsatidwe mosavuta,odandaula ayenera kulemba bwino-bwino zomwe akudandaulazo ndi kuwonetsetsa kuti zofunika ngati izi zalembedwa:

- Dzina
- Chaka , Mwezi ndi Tsiku lobadwa
- Mutu waukulu wa chidandaulo
- Dzina la nthambi ya boma yomwe akusumila
- Mapepala ndi makalata onse ofunika pa nkhaniyi
- Masiku ndi malo omwe zodandaula zinachitika
- Zomwe mwachitapo nkhani isanafike kwa Ombudzimani monga kudziwitsa akuku-akulu ena ku nthambi yosumilidwa za chidandaulochi
- Zina zomwe zachitikapo pa nkhaniyi
- Nambala ya chitupa cha ntchito
- Keyala ndi manambala yanu ya lamya

Ofesi ya Ombudzimani Mukhoza Kuyipeza Motere:

Lilongwe (Likulu la Ofesiyi)

St Martins House

Private Bag 348,

LILONGWE 3

Tel: (265)01774899/866

Fax:(265)01774958

Lilongwe (Ofesi la Chigawo Chapakati)

St Martins House,

Private Bag 348,

LILONGWE 3

Blantyre (Ofesi la Chigawo cha Kum'mwera)

Kannabar House

Private Bag 171,

BLANTYRE

Tel (265)1833317

Mzuzu (Ofesi la Chigawo Cha Kum'mpoto)

Mpico House

Private Bag 12,

MZUZU

Tel./Fax: (265) 1334726

Balaka (Ofesi la Chigawo cha Ku M'mawa)

P.O Box 150,

Balaka.

TEL:(+265)111624912

THANDIZO LA OFESI YA OMBUDZIMANI NDI LA ULELE

OFESI YA OMBUDZIMANI

UPHOLDING FAIRNESS, GOOD GOVERNANCE AND RULE OF LAW

KUTETEZA ANTHU KU ZIPSYINJO ZODZA CHIFUKWA CHA KAGWIRIDWE KA NTCHITO KOSAYENERA NDI KOSOWA CHILUNGAMO PA NTCHITO ZA BOMA

Ombudzimani

Ombudzimani ndi ofesi yotumikira anthu yomwe ndiyoyima payokha ndipo inakhazikitsidwa kudzera m'malamulo akulu a dziko lino komanso ku lamulo lovomerezedwa ndi nyumba ya malamulo kuti izifufuza ndi kuthandiza anthu omwe ali ndi chidandaulo chochuza kupondelezedwa, kusalabadiridwa kapena kusowa chilungamo pa ntchito ina iliyonse ya boma komanso nthambi zake

Ofesiyi ndi imodzi mwa nthambi zotumikira ndi kuthandiza anthu pa nkhani za chilungamo ndi malamulo yomwe inakhazikitsidwa ngati chimodzi mwa zofunika pa ntchito yolimbikitsa ufulu wa anthu wa demokalase ndipo inayamba ntchito zake mchaka cha 1995, patangopita nthawi yochepa mdziko muno mutayamba ndale za zipani zambiri.

Ntchito za Ofesiyi

- Kumva madandaulo kuchokera kwa anthu
- Kufufuza madandaulowa
- Kupeleka chigamulo pa nkhani yomwe yafufuzidwa

Mphamvu za Ofesiyi

Kuti igwire ntchito zake bwino, ofesi ya Ombudzimani inapatsidwa mphamvu zotere:

- Kupeza njira yoyenera ya mmene nkhani iliyonse ingafufuzidwilidwe
- Kuyitana, kudzera mu chisamani, munthu wina aliyense amene akukhuzidwa ndi nkhani iliyonse yomwe ikufufuzidwa kuti adzapeleke umboni
- Kulamula munthu ndi ofesi iliyonse kuti itulutse poyela ma kalata komanso umboni wina uliwonse ofunika pa nkhani yomwe ili kwa ombudzimani
- Kufunsa mafunso munthu wina aliyense yemwe akukhuzidwa ndi ndi nkhani yomwe ikufufuzidwa
- Kulumbilitsa munthu wina aliyense asanapeleke umboni pa mulandu otsimikiza kuti umboni omwe atapeleke ndi owona
- Kufunsa khothi kuti liyimbe mulandu ophwanya malamulo a dziko lino kwa munthu wina aliyense osalabadira chisamani, chigamulo ndi mfundo inayiliyonse ya ofesiyi

Madandaulo Opita kwa Ombudzimani

Ofesi ya Ombudzimani imamva ndi kufufuza madandaulo okhuza zipsyinjo, kusowa chilungamo, chipongwe ndi kusalabadiridwa komwe munthu wina aliyense wakumana nako kuchokera ku ma ofesi a boma ndi nthambi zake pa ntchito zawo. Izi ndi monga pamene ogwira ntchito za boma wachita izi: Kutenga nthawi yayitali asanathandize munthu ofuna chithandizo , kusatsata malamulo oyenera, kugwiritsa mphamvu za ntchito yake molakwika ndinso kuphwanya ufulu wa chibadidwe wa munthu wina aliyense

Madandaulo amene a Ombudzimani Safufuza

- Madandaulo okhuza ma ofesi ndi ntchito zomwe sizaboma
- Milandu yomwe imagamulidwa kale ndi a khoti ya malamulo
- Milandu yomwe ili kale m'manja mwa nthambi zina za malamulo
- Madandaulo omwe angathe kuwunikidwa ndi kugamulidwa bwino ndi a khoti

Zotsatira Kufufza kwa Ombudzimani

Malingana ndi zomwe yapeza mukufufuza kwake, ofesi ya Ombudzimani itha kuchita izi pa chidandaulo china chilichonse:

- Kugamula kuti chiganizo cha nthambi ya boma ndi chosayenera ndipo chiletsedwe
- Kugamula kuti chiganizo cha nthambi ya boma ndi choyenera ndipo chipitilire
- Kugamula kuti chidandaulo chomwe munthu anapeleka ku ofesiyi ndi chosayenera
- Kupeza njira ina yoyenera yomwe nkhani iliyonse ingathetsedwere
- Kulangiza odandaula za njira zina zomwe angapezele chilungamo mzidandaulo zawo
- Kutumiza milandu kwa nthambi zina za malamulo za boma zoyenera monga ku ofesi ya mkulu oweruza milandu ya Director of Public Prosecution ndi ena
- Kubweretsa odandaula ndi oyankha milandu pamodzi kuti athwe kupeza yankho pa nkhani kudzera mukukambirana

Kuphwanya Malamulo a Ofesiyi

Munthu wina aliyense ath kuyimbidwa mulandu ophwanya malamulo a ofesi ya Ombudzimani ngati atachita izi:

- Kulephera kukawonekera popanda chifukwa chomveka pamene wayitanidwa kuti akapeleke umboni ndi kuyankha mafunso kuchokera ku ofesiyi
- Kukana kulumbitsidwa asanayambe kufunsidwa mafunso ndi ofesiyi
- Kukana kupereka umboni ndi zoyenera zina zofunika ku ofesiyi pamene ikufufuza nkhani
- Kulepheretsa ogwrira ntchito ku ofesiyi kugwira ntchito zawo
- Kuopseza odandaula ndi munthu wina aliyense amene akukhudzidwa ndi nkhani imene ili m'manja mwa ofesiyi
- Kusikoneza zochitika pamene ofesiyi ili mkati momva nkhani

Chilango

Munthu wina aliyense opezeka olakwa pa mulandu ophwanya lamulola ofesi ya Ombudzimani adzalamulidwa kuti apelike chindapusa cha ndalama zokwana K10000 kapena kukakhala ku ndende kwa zaka zisanu. Olakwayu akhonzanso kulamulidwa kuti apelike chindapusa ndi kukagwira ukayidi zonse pamodzi